Mayina a mpingo ndi mamembala ake.

Zipembedzo nthawi zambiri zimavala dzina la munthu omwe adayambitsa mpingo. Nthawi zina amavala dzina la chiphunzitso. Ena amavala dzina la Malo amene Mpingo udayambira. Mpingo wa m'Baibulo umaremekeza Mulungu ndi dzina lake. Umatchedwa "***mpingo wa Mulungu"***(1 Akorinto 1:2) ndi ***"mpingo wa Khristu"***(Mateyu 16:18;Aroma 16:16). Mamembala amatchedwa ***"ophunzira"*** chifukwa ndi ophunzira a Yesu(Machitidwe 16:1). Amatchedwaso***"oyera mtima"*** chifukwa adapatulidwa ku dziko lapansi (1 Akorinto 1:2, Afilipi 1:1). Amatchedwaso***"ana a Mulungu"*** chifukwa amakhala kuti anabadwa mwatsopano mu banja lake (Yohane 3:3-5; 1 Yohane 3:1). nthawi zina amatchedwa ***"okhulupirira***" chifukwa amakhulupirira mwa Yesu Khristu kuti adzawapulumutsa(Machitidwe 5:14; Yohane 8:24). Iwo ali ***"ziwalo"*** chifukwa cha ubale wawo wina ndi mzake mu thupi (1 Akorinto 12:27). Mamembala a mpingo wa m'Baibulo amatchedwaso "***akhristu"***. Mneneri Yesaya analosera kuti Mulungu adzapatsa anthu ake dzina latsopanoli (Yesaya 62:2; Machitidwe 11:26; Machitidwe 26:28; 1 Petro 4:16).

Kulowa mu mpingo umodzi woona.

Munthu amalowa mu mpingo woona ndi kumvera Uthenga Wabwino(Aroma 6:16-18; 1 Petro 1:22,23). Kumvera kumeneko kumaphatikiza kumva mawu a Mulungu (Aroma 10:17), kukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi mwana wa Mulungu(Marko 16:16), kulapa machimo onse (Machitidwe 2:38), kuvomereza Yesu Khristu kuti ndi mwana wa Mulungu(Mateyu 10:32,33), kuikidwa m'manda mwa ubatizo kuchotsa machimo (Aroma 6:4; Agalatiya 3:26,27). Pamene munthu amvera malamulo amenewa Mulungu amamuonjezera iye ku mpingo wake (Machitidwe 2:47; 1 Akorinto 12:12).

FOR MORE INFO CONTACT;

rdgmissions@charter.net

www.icotb.org

MPINGO UMODZI WOONA

Pali zipembedzo zosiyanasiyana (mipingo yopangidwa ndi anthu)! Zonse zili ndi oyambitsa osiyana. Zonse zinayamba nthawi ndi malo osiyanasiyana. Chipembedzo china chiri chonse chimavala dzina losiyana ndi la mzake. Aliyense amalambira m'njira yake. Zipembedzo zimasiyanaso pa utsogoleri. Amaphunzitsa ziphunzitso zosiyanasiyana. Amaphunzira njira zosiyanasiyana mmene anthu angapulumutsidwire. Mzodabwitsa kuti awo amene amati amakhulupirira Baibulo amavomereza kusokonezeka koteroko. Anthu ambiri samafunsa pa nkhani imeneyi. Ena amawilingula ndikumanena: "Tonse tikupita kumwamba. Tikupita koma tiri mu nsewu wosiyanasiyana." Ena amati: "Mpingo wina uli bwino monga wina." " Lowani mu mpingo umene mwasankha."

Kodi Mulungu ali nako kusankha? Pali mpingo wobvumbulutsidwa mu Baibulo? Ngati Yesu anakhazikitsa mpingo, kodi ife sitiyenera kukhala Malo mwa umodzi woyambitsidwa ndi munthu? Kodi Baibulo limati chiyani?

Baibulo limaletsa Magawano.

Yesu anapemphera kuti onse amene akukhulupirira mwa Iye akhale amodzi(Yohane 17:20-23). Paulo anadzudzula mpingo wa ku Korinto chifukwa chogawanika: ***"koma ndikudandaulirani Inu, abale, mwa dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti munene chimodzimodzi inu nonse, ndi kuti pasakhale malekano pakati pa Inu: koma mumangike mu mtima womwewo ndi m'chiweruziro chomwecho"*** (1 Akorinto 1:10). Akhristu amalamulidwa kuyang'anira iwo omwe akuyambitsa magawano pophunzitsa chiphunzitso china(Aroma 16:17,18).

Mpingo umodzi wokha.

Yesu analonjeza: "***pa thanthwe ili,ndidzakhazika mpingo wanga"*** (Mateyu 16:18). Sanalonjeze kuti adzakhazikitsa zipembedzo zambiri! Analonjeza kukhazika mpingo wake! Adafera Mpingo wake (Machitidwe 20:28; Aefeso 5:25). Palibe pamene Baibulo limati Yesu anamanga zipembedzo! Ndiponso Baibulo siliphunzitsa kuti Yesu anafera mpingo uliwonse wokhazikitsidwa ndi munthu! Anafera mpingo umodzi, umodzi umene anaugula ndi mwazi Wake. Mpingo ndi thupi la Khristu (Aefeso 1:22-23). Pali thupi limodzi(Aefeso 4:4). Chomcho, Pali mpingo umodzi! Yesu ndi Mpulumutsi wa thupi lake (Aefeso 5:25). Ngati tikufuna kupulumutsidwa, tikuyenera kukhala mthupi lake. Sitingapulumutsidwe mu mipingo yopangidwa ndi anthu.

Mpingo unayamba ku Yerusalemu mu A.D. 33.

Yesu analonjeza kukhazika mpingo wake(Mateyu 16:18). Aneneri analosera kuti mpingo udzayamba mu ***"masiku otsiriza"*** ku Yerusalemu(Yesaya 2:2,3; Yoweri 2:28-32). Yesu anauza Atumwi ake kuti akadikire Mzimu Woyera ku Yerusalemu(Machitidwe 1:4-8). Mzimu unadza pa iwo tsiku la Pentekoste(Machitidwe 2:1-13). Petro anati uku kunali kukwaniritsidwa kwa ulosi wa Yoweri (Machitidwe 2:16-21). Analalikira Uthenga Wabwino kwa anthu. Pamene anamva, kukhulupirira, kulapa ndi kubatizidwa, ndipo anaonjezedwa mu mpingo wa Ambuye(Machitidwe 2:22-47). Onse lero amene amvera Uthenga wofanana m'njira imodzimodziyo akuwonjezedwa ndi Ambuye ku mpingo womwewo!

Yesu ndiye Mutu.

"***Ndipo Iye ali mutu wa thupi,mpingowo; ndiye chiyambi, wobadwa woyamba wotuluka mwa akufa; kuti akhale Iye mwa zonse woyambayamba"***(Akolose 1:18). Sitiwerenga m'Baibulo za mutu wina wa mpingo. Palibe mlaliki,m'busa,wansembe,papa,pulezidenti,gulu,kapena komiti pa mpingo umodzi woona. Yesu yekha ndiye mutu! Likulu la mpingo umodzi woona liri kumwamba kumene kuli mutu ndiye Yesu Khristu(Machitidwe 2:33-36).

Mpingo wina uliwonse wa Yesu Khristu ndiodziimira pa okha.

Pamene kuli thupi limodzi, akhristu m'madera onse amasonkhana pamodzi kuti alambire. Paulo analembera akhristu a ku Roma kuti: ***"mipingo ya Khristu ikupatsani moni"***(Aroma 16:16). Iye sanali kunena za mipatuko yosiyanasiyana, koma za misonkhano ya akhristu m'dera liri lonse. Awa pamodzi amapanga thupi la Khristu. Paulo analembera oyera mtima a ku Korinto kuti "***mpingo wa Mulungu umene uli ku Korinto"***(1 Akorinto 1:2). Anapempha akulu a mpingo wa ku Efeso kuti akumane naye pa Mileto(Machitidwe 20:17). Analankhura za **"*mipingo ya ku Galatiya"*** kutanthauza mipingo ya Khristu mu mzinda uliwonse wa Galatiya (Agalatiya 1:2).

Kupatula Khristu amene akulamulira kuchokera kumwamba,palibe bungwe la pakati la mpingo woona. Mpingo uliwonse umadziimira pawokha ndipo sudalira ena onse. Uliwonse uli ndi akulu a mpingo ake omwe amatchedwa a Bishopu(amatchedwaso oyang'anira komaso Abusa). Mpingo wa ku Antiokeya unatumiza thandizo kwa akulu a mpingo wa ku Yerusalemu(Machitidwe 11:29,30). Paulo ndi Barnaba ***"anasankha akulu mu mpingo uli wonse"(***Machitidwe 14:23). Paulo anaitana akulu a mpingo wa ku Efeso(Machitidwe 20:7). Analembera oyera mtima a ku Filipi ***"ndi oyang'anira(a bishop) ndi atumiki***"(Afilipi 1:1). Akulu amangoyang'anira mpingo umene iwo ali mamembala ake(1 Petro 5:1,2).

Pali dongosolo la Kupembedza

Mpingo wa m'Baibulo umakumana tsiku loyamba la sabata(Machitidwe 20:7; Akorinto 16:1,2). Amapembeza mu ***"Mzimu ndi mchoonadi"***(Yohane 4:24). Amadya m'gonero wa Ambuye(Mateyu 26:26-29; Machitidwe 20:7; 1 Akorinto 11:23-26). Amayimba nyimbo mosagwiritsa ntchito zida(Aefeso 5:19;1 Akolose 3:16; Ahebri 13:15). Amapemphera kwa Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu(1Timoteo 2:1-8). Amamva ulaliki ndi kuphunzira mawu a Mulungu(Machitidwe 2:42; 20:7; Mateyu 28:20). Amapereka potengera ndi mmene Mulungu wawapindulitsira(1 Akorinto 16:1,2).